The Baptist Tabernacle of Los Angeles

1329 South Hope Street, L.A. Civic Center

Mailing Address:
P. O. Box 15308
Los Angeles, CA 90015

Phone: (213) 744-9999

E-mail: rlhymersjr@sbcglobal.net

www.sermonsfortheworld.com

www.baptisttabernacle.com

Dr. R. L. Hymers, Jr.
Founding Pastor

Dr. Christopher L. Cagan
Pastor

Disembala, 2019

Okondedwa Anzanga:

Ndikanakonda ndikanakutumizirani kalata ya Krismas ya chisangalaloko. Koma, kunena zoona, Ndikukuuzani kuti chaka ndi theka zapitazi takumana ndi mpatuko waukulu. Mpingo kugawanikana.

Zidayamba miyezi ingapo tisanayambe chaka chatha. Dikoni wathu wa mkulu adayamba kupanga timaupo tamseri ndi mbusa wina. Awiriwo anapangana njira zoonongera mpingo wathu. Ndipo awiriwo anapangana kuti ayambitse mpingo wina ndi kutenga anthu ambiri monga m'mene akanathera kuchoka kwa ife. Pamene ndimadzazindikira za izi ndinali nditachedwa kale anthu anali atagawanikana kale.

Zadayamba pamene dikoni wosayamika anayesetsa kuti ndikangane naye kuti mpaka tifike "poponyerana zibakera." Pamene ndinakana kuchita ndewu, adachoka mu mpingo. Kenaka enanso anamutsatira. Wa pampando wa ma dikoni anayika zithunzi zolawula pa tsamba la intaneti lake. Wina wa "opandukawo" anayesetsa kundinamizira ine kuti zithunzizo zinali zanga, mpaka a polisi anakhudzidwa. Wapampando wa madikoniyu ndi mkazi wake anachoka mu mpingo.

Panthawi imeneyi, wa mkulu wa ma dikoni anayamba kujijirika. Anasiya mpingo wathu nayamba kukoka anthu ambiri m'mene anathere. Pakuti dikoni wa mkulu ameneyi wakhala ali mtsogoleri kwazaka zambiri, anthu ambiri anamtsatira ndikusiya mpingo wathu. Pamene mpatukowu umatha, anali atakwanitsa kukoka anthu kuposa theka.

Panthawi ngati iyi mabvuto a mthupi mwanga anayamba kuonekera ndipo sindinathenso kulalikira muma ulaliki onse awiri a la Mulungu. Mwana wa sukulu ya za Baibulo ndi amene amalalikira la Mulungu m'mawa uliwonse. Koma anali wosakhwima kuima nane pamene anzake ambiri anali atachoka mu mpatuko. Pa Febuluwale, 20 mnyamata ameneyu anandisiyanso. Iyeyo ndi amai ake anachoka mu mpingo nayamba kusonkhana ndi mipingo yina ya chivangeli yatsopano. Izi zinandikwana, pakuti ndimayembekezera kuti mlaliki wachinyamata ameneyu akhala mzanga wa pafupi nane. Pa Febuluwale 23, ndinasiya kukhala mbusa ndipo Dr. Christopher Cagan anakhala mbusa watsopano. Ine ninakhala mbusa wopuma. Ndinali wofoka kwambiri kuti ndizisonkhana nawo mu mpingo. Pa Malichi 3, Dr. Cagan analengeza kuti ndipume ndi kudzisankha yekha mbusa. Dr. Cagan ndi M'Kristu wa mphamvu, kusiyana ndi Mbusa Wurmbrand. Popanda utsogoleri wake mpingo wathu siukadapulumuka.

Komabe zinthu za bwino zinapitirira kuchitika. Pa Januwale 26 chilankhulo cha chi 41 chinawonjezereka ku tsamba lathu la intaneti. Tsiku lomwero la pa (Januwale 26) "app" yathu inakhazikitsidwa pa iphone ndi Android. Kuyambira pomwepo anthu mazana-mazana padziko lonse la pansi a lumikizana nafe kudzera mu "app," tikuthokoza chifukwa cha mzathu, wa mishoni kwa anthu a chi Yuda amene amakhala mu mzinda wa New York. Kenaka chilankhulo cha chi 42 chinawonjezekera – chilankhulo chodziwika ku Malawi kumene ndi ku Afrika. Pa Febuluwale 23, Dr. Cagan anakhala mbusa wokhazikika ndipo ine ndinakhazikitsidwa kukhala mbusa wopuma.

TSAMBA LATHU LIKUPEZEKA NDI ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDI AWIRI PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.

Sitichita kusoweka kunena kuti, ndinali wofoka chifukwa cha kunzunzika m'maganizo malinga ndi zonse zinachitikazi. Ndiri wothokoza kwambiri chifukwa cha mkazi wanga amene anaima nane pamene ndimadutsa mu zonsezi. Kuyambira Febuluwale 27 mpaka Malichi 20 ndinapitanaye ku tchuthi ku Arizona kuti tikapume. Pa Malichi 20, ndinabwerako ndikumadzalalikira la Mulungu madzulo aliwonse ndi kumaphunzitsa loweruka madzulo aliwonse.

Kuyambira pamenepo nyumba yopemphereramo tinayiika pa malonda. Pa Epulol14 chisangalalo cha kukumbukira zaka 78 zanga zakubawa chinachitikira ku nyumba yakale. Pa Meyi 7 ndinayambitsa maphunziro a kuyamba kwa chikhulupiriro kwa achinyamata okhulupirika a mu mpingo mwathu, pogwiritsa ntchito kabuki ka "Kulalika mwa Mphamvu". Kuyambira pa Meyi 22 mpaka 29, Dr. Cagan anatitenga mkaziwanga ndi ine kupita ku San Francisco kuti tikayendere mpingo wa Chinese Baptist ndi mbusa wao wa bwino. Tinakumananso ndi Mike ndi Mona Riley, mbusa mzathu wakale kwambiri wa mpingo umene ndinayambitsa ku Marin County. Mike anandirimbikitsa kwambiri, ndipo anandiitana kuti ndikatumikire pa mwambo wokumbukira kuti mpingo watha zaka 50. Anthu ena andinyogodola , ine chifukwa cha mpatuko womwe unachitika ku mpingo wathu, zimene zimandipangitsa kuti ndimve kuwawa kwambiri.

Pa Julayi 28 tinali ndi phwando pa mpingo wathu lokumbukira kuti Dr. Cagan wakwanitsa zaka 66 zakubadwa. Pamenepo zinalengezedwa kuti mpingo wathu tsopano wa pa San Gabriel Valley uzitchedwa, "The Chinese Baptist Tebernacle of Greater Los Angeles." Tagula nyumba yatsopano kumeneko ndipo kulemba kwa zikalata za umwini wa malo kumalizika posachedwapa.

Kumapeto kwa Julayi ndinatenga Mai Hymers kukapumanso kunyanja. Mkaziwanga, Ileana, mosakaika ndi mai busa wabwino kwambiri mdziko lonse lapansi. Mwana wanga wa mwamuna Robert Leslie ndi ine tinamutumiza ku Israel kuti akapitidwe mphepo. Pa Novembala 17 ndinayamba ziphunzitso zotsatana za m'mawa wa la Mulungu ndi madzulo. Ndinthawi yoyamba kuti nditumikire ndi mphamvu mu nthawi zonse ziwiri pa tsiku la Mulungu patatha nthawi yaitali. Pansi pa utsogoleri wa Dr. Cagan ndi kulimbikira kwake, achinyamata a wiri apulumutsidwa, ndi ana asukulu ambiri a chi Chinese ayamba kubwira ku mpingo. Dr. Cagan anafika mpaka pogulitsa nyumba yake ku Los Angeles, ndipo akuyang'ana nyumba ina pafupi ndi nyumba ya San Gabriel. Tisamutsira mpingo wathu ku nyumba yatsopanoyi mu masiku ochepa akubwerawa.

Mpatuko ukuoneka kuti watha. A City of Hope anandiuza masiku apitawa, kuti Khansa amene anandipeza naye akuoneka kuti wa chiritsidwa. Dr. Cagan, mkazi wanga ndi ine tinakonza phwando lothokoza kunyumba kwathu pamodzi ndi anyamata athu ndi zidzukuru zathu, ndi ambiri mwa amene anaima nafe mu nthawi ya chimsautso. Tinari ndi nthawi yabwino kwambiri pamodzi!

Ambuye akudalitseni nonse! Chonde kumbukirani kutipempherera pamene tikuyamba mpingo wa chi Chinese!

Ndiri wonyadira chifukwa cha banja langa. Kuchoka ku manzere kupita kumanja, Wesley, Leslie ali ndi khanda Hannah, ine, Ilena ali ndi khanda Sarah, mkazi wa Leslie Jin, Mai ake a Ileana Linda ndi mchimwene wake Erwin Cuellar.

Yesu Kristu mpulumutsi wathu alemekezeke!



R. L. Hymers, Jr.,
D.Min., Th.D., Litt.D.
Afilipo 4:13

"Ndikadapanda kukhulupirira kuti ndikaone ubwino wa Yehova mdziko la amoyo, ndikadatani! Yembekeza Yehova: Limbika, ndipo Iye adzalimbitsa mtima wako; Inde, yembekeza Yehova" (Masalmo 27:13-14).

TSAMBA LATHU LIKUPEZEKA NDI ZIKWI-ZIKWI ZA MA ULALIKI MU ZILANKHULO MAKUMI ANAYI NDI AWIRI PA WWW.SERMONSFORTHEWORLD.COM.